


# AHEBRI, MUTU WACHIWIRI <sup>1</sup>

 Ndinali kuno mu kalasi ndipo ndinakomedwa... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Ndipo tsopano Bukhu loyamba la Ahebri, ndi Paulo, ife tinapeza, kapena ife tikukhulupirira. Afioroje ali pa mapeto; iwo sakudziwa basi kuti ndi chiti, kapena yemwe analilemba Ilo. Koma, ine ndikukhulupirira, aliyense ali ndi kuzindikira pang'ono kwauzimu angakhoze kuwona kuti anali Paulo. I—izo zimakhulupiridwa, ndi ambiri a olemba, kuti ndi Paulo. Ndi momwe kuti iye. . .

<sup>2</sup> Mu mutu woyamba, ife tinapeza kuti unali kuwakweza Ambuye Yesu. O, momwe iye anazisitsira pansi, kuti atisonyeze mwa—mwa chomuchitikira chimene iye anali nacho pa ulendo wake waku Damasiko. Tsopano, Paulo anali, pa kuyamba nazo, wafioloje weniweni. Paulo anaphunzitsidwa pansi pa Gamalieli, mmodzi wa aphunzitsi opambana a tsiku limenelo. Ndipo iye anali wanzeru ndi waluntha, ndipo iye anali sikolala wothyathalyika kwenikweni wa Baibulo.

<sup>3</sup> Ndipo ine ndinapeza izi, pamene iye anali paulendo wake kupita ku Damasiko, ali ndi makalata mthumba mwake, kuti akawamange onse awo omwe anali mu njira yodala yakale ya Uthenga, ndipo munthuyo anali wodzipereka. Koma, ine nthawizonse ndakhala ndikukhulupirira kuti kuchokera pomwe Paulo anamuwona Stefano akufa, ine ndikuganiza kuti izo zinamukhudza iye. Pamene iye anavomerezera ku imfa ya Stefano, ndipo iye anagwirizira zikhotho za iwo omwe ankamugenda iye, ndiye Paulo anali pa mulandu wa magazi a Stefano. Ndipo iye anavomerezera, ndipo anati, “Ine sindiri woyenera nkomwe,” anati, “chifukwa ine ndinakhetsa magazi a Wake—a Wake, wofera, Stefano. Chifukwa, iye anachitira umboni kwa izo.

<sup>4</sup> Ndipo ngati inu muchitira umboni kwa chirichonse, ndinu wolakwa basi monga wochita nawo icho. Chotero ngati ife tichitira umboni, kumati, “O, inde, iwo samayenera kuti achite izo, izi *mwakuti-n-mwakuti*.” Muzikhala osamala zomwe inu munena, chifukwa ndinu olakwa momwe kuweruza kwanu kupitira. Ngati inu simungathe kulingalira, musati muzinena kanthu, muzingozisiya izo zokha. Ndiye pamene inu muchitira umboni kuti ndinu Mkhristu, ndiye ndinu wolakwa. Mukuona? Muli ndi mulandu wa kukhala Mkhristu, ndipo inu muyenera kuti muzikhala moyo wa icho. Ndipo pamene Mulungu apanga—lonjezo mu Baibulo. . . Ine ndikumuwona bambo apa mu chikuku. Pamene Mulungu apanga Lonjezo, Iye amakhala wolakwira Lonjezo limenelo mpaka Iye atalifikitsa Ilo pochitika. Mulungu ali pa mulandu pamene Iye apanga Lonjezo.

Ndipo Malemba ali pa mulandu mpaka iwo atakwaniritsidwa. Mukuona? I—iwo ali apo pomwe ng—ngati neno lomwe Mulungu walipanga. Ndipo Iwo ayenera kuti akwaniritsidwe kapena Mulungu ali ndi mulandu. Mukuona?

<sup>5</sup> Ndipo chotero Paulo, pokhala mphunzitsi, ndi pakubwera pa ulendo wake waku Damasiko tsiku lijali, pafupi, cha mu nthawi ya dzuwa liri pamutu, ine ndikulingalira. Apo panali Kuwala kwakukulu kunawala kuchokera Kumwamba, ndipo Iko kunamuchititsa iye khungu, ndipo i—iye anagwera pansi. Ndipo iye anati iye ankafuna kuti adziwe Yemwe iye anali. Iye anati liwu linayankhula, ndipo linati, “Saulo, Saulo, bwanji iwe ukundizunza Ine?” Ine ndikukhulupirira mutu wa 8 wa Machitidwe.

Iye anati, “Nndani Uyo yemwe ine ndikumuzunza?”

<sup>6</sup> Ndipo Liwu linabwerera, ndipo linati, “Ine ndine Yesu.” O! “Ine ndine Yesu, ndipo ndi kovuta kuti iwe uzimenyana ndi zisonga.” Ndipo kodi Yesu anali chiani apo? Yesu, Iye anali Kuwala, Kuwala kwakukulu basi kukuwala mowala.

<sup>7</sup> Tsopano kuti zitilimbikitse ife ndi kupeza maziko apa. Kodi Iye anali Kuwala bwanji, pamene Iye anali Munthu? Tsopano, palibe wina . . .

Apo panali gulu la asilikari ali ndi Paulo, olondera ku kachisi, akupita uko kuti akawamange. Paulo anali woyang’anira wamkulu. Ndipo iwo anali kupita uko kuti akawamange anthu amenewo, chifukwa cha misonkhano yawo yokopa ndi zina zotero, ndi chifukwa cha ziyembekezere zawo zachipembedzo zomwe zinali mwa iwo.

<sup>8</sup> Koma, tsopano, apa panali Yesu ngati Kuwala kwakukulu. Tsopano, ngati inu mukukumbukira, pachiyambi, Yesu anali Kuwala. Yesu anali Logos yomwe inatuluka kuchokera kwa Mulungu. Ndipo Iye anali . . . Iye anali Mngelo wa Pangano yemwe anawatsogolera ana a Israeli kudutsa mu chipululu. Ndipo Iye anali Lawi la Moto lomwe iwo ankayang’anapo. Ndipo Iye anali . . . Ndipo pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo ine ndikubwerera kwa Mulungu.” Chotero ngati Iye anabwera kuchokera ku Lawi Lamoto, kudzakhala mwa Munthu, ndiye ngati Iye anabwerera kumene Iye anali, Iye anabwereranso kwa Kuwala kachiwiri. Ndipo apo Iye anali pamene Paulo anamuwona Iye, Iye anali Kuwala.

<sup>9</sup> Tsopano, asilikari onse awo omwe anali ndi Paulo sanakuwone Kuwalako. Ndiye kodi ndi zotheka kuti wina angakhoze kukuwona Iko ndipo enawo nkusakuwona Iko? Ndithudi. Chabwino. Iye, Paulo, anakuwona Iko, koma ena onse a iwo sanakuwone Kuwalako.

<sup>10</sup> Tsopano, pamene Petro anali mu ndende, ife tikupeza kuti Kuwala uku kunabwera mu ndende, kunatsegula zitseko.

Ndipo iye anali...Kuwala uko kunawachititsa khungu asilikali ena onsewo, pamene iwo anali kuyenda akutuluka, Petro akupita. Ndipo pamene iye anafika pa chitseko, icho chinangotseguka chokha, mwakachetechete, chinatseka pambuyo pake. Kuchokera mndende yamkati, iye anapita ku chitseko chakunja. Icho chinatsegula mwa chokha, chinatseka mwakachetechete. Ndiyeno iye anapita mu mpatawo, anapita kunja mu msewu wa mzinda. Ndipo iye anasisita maso ake, ngati kuti ati, “Kodi ine ndimalota?” Iye sankadziwa zomwe zinali zitachitika. Koma, Mngelo wa Ambuye, Mngelo yemwe uja yemwe anali Lawi Lamoto yemwe anamuyendetsa Mose mpaka ku nyanja ndi kuitambasula iyo apo, o, ndipo Nyanja Yakufa...Nyanja Yofiira inapanga makoma ku mbali zonse, ndipo Israeli anadutsa pamenepo.

<sup>11</sup> Ndipo pamene iwo anafika ku Yordani wofufuma, Iye sanadziwonetsere Yekha mowoneka apo. Koma Iye anali apo, chifukwa Iye anangoitsegula iyo apo. Ndipo iwo anawoloka mu Epulo, pamene zigwa zonse zinali zitadzadza ndi madzi. Ndipo Iye analeketsa kasupe, ndipo Iye analeketsa chisanu kuti chisasungunuke, chifukwa iyo siinapange khoma mokwera ndi kukwera; iyo inangoima. Uyo ndi Yehova wathu. Uyo ndi Ambuye wathu Yesu. Inangoima; ndipo iwo anayenda nawoloka pa nthaka youma.

<sup>12</sup> Tsopano, Mulungu analonjeza kuti Iye akanamawasamalira iwo, kotero Iye anali wokakamizidwira ku Lonjezo Lake. Tsopano, Paulo, pozindikira za zinthu izi, ndi kuzidziwa izo, iye anali nawo mwayi, chifukwa Mulungu anali kuyankhula molunjika kwa Paulo. Iye sanali kuyankhula kwa asilikari omwe anali ndi iye. Iye anali kuyankhula kwa Paulo yekha.

<sup>13</sup> Tsopano, pamene—pamene Mngelo wa Ambuye anabwera pansu, mwa mawonekedwe a nyenyezi; ndipo oyang’ana nyenyezi, amuna anzeru aku India, pamene, iwo anawona Nyenyezi Iyo ndipo anaitsatira Iyo kwa mailosi mahandiredi. Ndipo Iyo inadutsa moyang’anira mmwamba mulimonse, chifukwa iwo ankasunga nthawi mwa nyenyezi. Ndipo palibe mmodzi yemwe anaiwona Nyenyezi iyo koma amuna anzeruwo. O, mai! Kodi izo sizikukukondowezani inu? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>14</sup> Ndiye, inu mukuona, Mulungu samachita ndi mabungwe. Iye samachita ndi magulu a anthu. Iye amachita ndi munthu payekha. Iye amadziulula Yekha kwa anthu payekha. Ndipo tsopano—tsopano kuti tinene izi, osati izi...Mulungu akudziwa mtima wanga. Ndipo sindikunena izi kwa inemwini, podzitamandira ndekha, tsopano; basi kuti ndikhale apo. Koma, kodi inu mumadziwa, Mulungu yemweyo, Yesu yemweyo, ali ndi ife mmawa uno? Kodi inu mukudziwa, aliyense wa inu ali nawo, umboni wa yekha pakali pano, kuti Iye ali pano? Ndipo wa...Iye watichitira ife chinachake mu tsiku lino chimene Iye

sanachichite mu masiku enawo; Iye wajambulitsa Chithunzi Chake mu tsiku lino. Ife tiri nacho Icho chapachikika *apocho*. Mukuona? Lawi la Moto, Ambuye Yesu yemweyo.

<sup>15</sup> Penyani momwe Iye akugwirira ntchito tsopano. Ngati Iye ali Ambuye Yesu yemweyo, Iye azichita zinthu zomwezo, pakuti Baibulo linati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

<sup>16</sup> Tsopano, Paulo asanalengeze chirichonse, ngati izi ziri zolondola kapena zolakwika, iye poyamba anapita ku Igupto ndipo anakakhalako zaka zitatu, kuti akapeze ngati izo zinali Mwamalemba kapena ayi. Kodi inu munayamba mwadziwa izo? Kutachitika kutembenuka mtima kwa Paulo, iye anapita ku Igupto kwa zaka zitatu. Uko iye anakakhala, ndipo uko ndi kumene iye anakaphunzira nzeru yaikulu iyi.

<sup>17</sup> Tsopano, osati mwa kufanizitsa kulikonse, ine ndikungokupatsani inu momwe Mzimu Woyera ukadali panobe mofanana. Tsopano, mpingo wanga kuno ukukumbukira, zaka zapitazo, pamene Mngelo uyu anakkhoza kuwonekera ndipo anakkhoza kuwonetsa zinthu. Ine ndinali wopenekera pang’ono pa Izo. Nonse a inu mukudziwa zimenezo, inu anthawi zakale. Ngati i. . . Ngati uko kuli kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu, pamene inu mwamva. Eya. Penyani, tayang’anani pa mpingo, komabe, kuchokera kwa anthawi-zakale. Mukuona? Ine ndinali wopenekera, chifukwa alaliki ankandiuza ine kuti Izo zinali za Mdierekezi. Ndipo ine ndinkakhala ngati ndinkazikhulupirira izo, koma ine ndinayembekezera. Ine sindinkanena kanthu pa Izo.

<sup>18</sup> Koma, o, lidalitsike Dzina la Ambuye! Usiku wina, kutsidyako, Iye anabwera pansu, Mngelo, ndipo anaulula Izo mu Malemba, kuti Iye anali. Ndipo pamene ine ndinaziwona Izo mu Malemba, ndiye nkuti ndilindime kudutsa mdziko ndi Iwo, Uthenga.

<sup>19</sup> Kuchokera pamenepo kwapita Oral Roberts, A. A. Allen, Tommy Osborne, Tommy Hicks, ndi ena ati. Mukuona? Ndi Uthenga wa kwa anthu.

<sup>20</sup> Ndipo Yesu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndi Mwamalemba, Iye ali yemweyo. Iye akuchita zomwezo. Iye ali yemweyo. Ndipo Iye akugwira ntchito mofanana. Iye akudziwonetsera Yekha mofanana. Ndipo Iye ali pano, mmawa uno, mofanana. Tsopano ife tikhoza kumuwona Iye; ife tikhoza kusamuwona. Chirichonse chomwe icho chiri, ife tiri nawo umboni pakali pano kuti Iye ali pano.

<sup>21</sup> Tsopano, ife tikupeza tsopano kuti, Paulo, pa chomuchitikira ichi, ndi pakulemba makalata awa, ochuluka a iwo, kuchokera mu ndende, iye anali atafanizitsa Chipangano Chakale kwa Chatsopano. Tsopano kumbukirani, mlembi wotsiriza wa Baibulo ili, mwa kudzoza, Mulungu anabwera pansu

ndipo anamuuya iye, “Ngati munthu aliyense adzawonjezera chirichonse kwa Ilo kapena kuchotsa chirichonse kuchokera kwa Ilo, mofanana adzachotsera gawo la mu Bukhu Lamoyo, kwa iye.” Chotero ife tisamayekeze kuwonjezera chinthu chimodzi kwa Iwo. O, Iwo ayenera kuti azikhala monga Iwo aliri, pasamakhale chirichonse chowonjezera kwa Iwo. Ndipo ife tiyenera kuti tizilimbanira chirichonse chomwe chiri mu Iwo. Ine sindikufuna china chowonjezerapo, ndipo ine sindikufuna chirichonse chocheperapo. Ine ndikufuna basi chimene Iwo akunena.

<sup>22</sup> Tsopano, Bukhu ili la Ahebri, chifukwa chomwe ine ndalisankhira Ilo; cholinga chimodzi, chinthu chimodzi; kalata iyi, “Wokonedwa M’bale Branham,” ndi zina zotero. Ndipo, i—i, ife tikufuna kuti tizikhala ndi Mawu.

<sup>23</sup> Tsopano, mutu woyamba, unali kumukweza kwa Yesu, kotero Iye ali Mmodzi wofunikirayo. Ndipo Paulo anatidziwitsa ife, usiku wina, kuti Iye anali mu chiyambi chachikulu. Ndipo ife tinapeza kuti Iye sanali kanthu kochepera “Melkizedeki, Mfumu ya Salemu,” Wamkulu wa mutu wa 7.

<sup>24</sup> Ndipo tsopano, mmawa uno, ife tikumuyandikira Iye kuchokera ku ena, pa maimidwe ena, kuchokera pa mutu wa 2. Tsopano, Paulo atatha kutipatsa ife Uthenga waukulu, wododometsa uwu, wa kumukweza Yesu, “Ndipo mpaka anawapanga Angelo kuti azimupembedza Iye.” Ndipo ine ndikuganiza, cha apa, monga dongosololo likuimira zakale, “Ndipo Iye adzalipiringiza ilo ngati chovala, koma ilo lidzatha, koma Iwe udzakhalapobe.”

<sup>25</sup> Ndipo cha mu mutu wa 2, ndime ya 2, ine ndikukhulupirira ndi pamenepo, “Masiku ano Iye akuyankhula kwa ife mwa Mwana Wake.” Ndipo, penyani, “Nthawi zamakezana ndi mmayankhulidwe osiyana Iye ankayankhula kupyolera mwa aneneri.” Ife tinadutsamo ndipo tinapeza chomwe aneneri anali, ndi momwe Mulungu ankabweretsa Uthenga Wake mwa aneneri. “Koma mu tsiku lotsiriza lino Iye wayankhula kudzera mwa Mwana Wake, Yesu, mwa Mzimu Woyera. Iye ankayankhula kudzera mwa aneneri, apo.” Ndiye ife tinabwerera mmbuyo ndipo tinadzapeza kuti, aneneri onse awo anali nawo Mzimu wa Khristu mwa iwo.

<sup>26</sup> Ife tinapita mmbuyo kwa Yosefe ndipo tinapeza kuti iye ankaimira mwangwiro Khristu. Tinapita mmbuyo kwa Mose ndipo tinapeza kuti ankaimira mwangwiro Khristu. Ndiye ife tinabwera mmusi kwa ngakhale Davide. Ndipo pamene Davide anakanidwa mu Yerusalemu, asakudziwa chifukwa chake, koma anapita pamwamba pa phiri ndipo anayang’ana mmbuyo ali pamwamba pa Phiri la Azitona, ndipo analirira pa Yerusalemu chifukwa iye anakanidwa. Zaka eyiti handiredi kuchokera apo, Mwana wa Davide anakanidwa ngati Mfumu, mu Yerusalemu,

ndipo anakhala pa phiri lomwelo nalira. O, Mzimu wa Khristu, ukuchita ndi aliyense payekha!

27 Tsopano, Paulo akuyambapo, kuti:

*Chotero ife tiyenera kuti tipereke tcheru chochuluka motsimikiza ku zinthu zomwe ife tazimva, . . .*

28 Mutu wa 2, tsopano, ife tikuyamba.

*Chotero ife tiyenera kuti tipereke tcheru chochuluka motsimikiza ku zinthu zomwe ife tazimva, kuwopa . . . nthawi iliyonse ife tingazilole izo kutipulumuka.*

29 O, Mulungu atafikitsa izo pachimake mu kachisi uyu mmawa uno. Ine ndikupemphera kuti Mzimu Woyera umize izo mwakuya kwambiri mu mitima yanu. “Ife tiyenera kuti tizipereka tcheru chochuluka motsimikiza kwa zinthu zomwe ife tazimva.” Kodi ife tiyenera kukhala anthu a mtundu wanji, pamene ife tikumuwona Yehova wamkulu akubwera pansu ndi kumachita zinthu zomwe Iye akuchitazi, ndi kumaziwona izo zikufanana, Lemba ndi Lemba, kuti izo ndi Choonadi? Ndipo ife timakhala apo nthawizina ngati bowa pa chipika, ndi basi osakhudzidwa choncho. Ife tiyenera kuti tizikhala otanganidwa, miniti iliyonse, kuyesera kuwatengera anthu kwa Khristu. Ife tiyenera kukhala miyala yamoyo. Ife tisamakhale konse ozengereza monga momwe ife tiliri. Ife timapita ku tchalitchi, ndipo ife timawawona Ambuye Yesu akuchita chinachake, k—kapena kutidalitsa ife mwanjira yotero, ndiyeno i—ife timabwerera mmbuyo ndi kumati, “Msonkhano wabwino kwambiri.”

30 Tsopano, kulalikira kwa Mawu, ife timasangalala nako, koma icho si chinthu chenichenicho. Si chimenecho. Ife tisamawapembedze Ambuye pamene tangotsiriza kulalikira kwa Mawu, monga ife nthawizonse timachitira, kumangomupembedza Iye. Izo nzodabwitsa. Koma ife tizimupembedza Iye ora lirilonse la moyo wathu. Pamene ife tiri ku ntchito, ife tizimupembedza Iye. Nthawi iliyonse mwayi ukazipereka wokha, tizimupembedza Ambuye pakuchitira umboni za Iye.

Ngati inu muwona, ena a inu madona, mukamuwona mkazi akulakwitsa, mpembedzeni Ambuye pakumutenga iye nkuti, “Mlongo, ulipo moyo wabwinoko kuposa uwu.”

31 Amuna inu ku ntchito yanu, pamene inu mumumva munthu akugwiritsa ntchito Dzina la Ambuye pachabe, tengerani mwayi ku mbali imodzi ndi kumupeza apo, ndi kumutenga iye padzanja, nkuti, “Inu, pali moyo wabwinoko kuposa uwu. Inu musamati muzigwiritsa ntchito mawu ajawa.” Ndipo muzimuuza iye mofatsa, mwanjira yaulemu. Zinthu zonsezo ndiko kupembedza.

Ndipo pamene ife timuwona wina akudwala, ndipo adotolo nkuti palibenso china chingakhoze kuchitidwa, ife tiyenera kuti tiziwapembedza Ambuye powauza iwo, “Alipo Mulungu wa Kumwamba yemwe amayankha pemphero.”

<sup>32</sup> Ndiyeno pamene ife tiwona zinthu izo zikuchitika, zomwe ife timaziwona zikuchitika mokwanira, ife tisamalole konse kuti zinthu zimenezo zitipulumuke. Ife timangozisiya izo zizitidutsa mzala zathu. Ndi lomwe liri vuto ndi mpingo wathu wawukulu wa Chipentekoste lero. Iwo alola kirimu ya zokolola yomwe kudutsa mzala zawo, pamene iwo anali nayo iyo mmanja mwawo. Koma, tayang’anani pa zomwe iwo achita, iwo achita monga mipingo ina yonseyo. “Iwo athamangira mu phindu, mu njira ya Kora, ndipo awonongeka; ndi njira ya Kaini, ndipo awonongeka mu zolankhula zokopa za Kora.”

<sup>33</sup> Iwo achita bungwe. Mmalo mokhala ndi ubale komwe ife tonse tingakhoze kukhala amodzi, iwo adzipanga okha bungwe. Apanga timabungwe tating’ono ndi timalingaliro tating’ono, ndipo tayambira kuchokera pamenepo ndipo angoswa ubale. Ndipo ngati inu simusamala, Abaptisti ndi Achipresbateria azitenga izo, chifukwa, “Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsira ana kwa Abrahamu.” Ndipo i—ife tazilola izo kuti zitipulumuke kuchokera mmanja pakukhala osagwirizana.

<sup>34</sup> Kodi Amwenye analiluzwa bwanji dziko lino kwa munthu wachizungu? Ndi chifukwa iwo anali osagwirizana. Ngati iwo akanapanga tsogolo limodzi lamphamvu...Koma iwo anali kumenyana wina pakati pa amzake ena. Iwo akanakhoza kugwira malo awo ngati iwo onse akanabwera palimodzi.

<sup>35</sup> Kodi ife tililuzwa chotani ilo? Chifukwa ndife osagwirizana. Timaluzwa chotani chotichitikira chathu ndi Mulungu, ndi chifukwa ife timakhala osagwirizana. Ife timakhazikitsa chimodzi, ndi kuchitcha *ichi m*—Methodisti, ndi *ichi* Baptisti, ndi *ichi* Assemblies, ndi *ichi* Umodzi, ndi *ichi china-chakenso*, ndi mpingo wa Mulungu, ndi Nazereni, Pilgrim Holiness. Ife tikuligawaniza Thupi la Khristu. Ife tisamakhale konse ogawanikana. Ife tikhoza kusiyana mu malingaliro, koma tiyeni tikhale abale a mtima-kwa-mtima. Mulungu akufuna kuti ife tikhale. Iye anafera Mpingo wonse wa Mulungu. Ndipo ife sitikufuna kuti tikhale ogawanizikana.

*Tsopano ife tiyenera kuti tipereke tcheru chochuluka motsimikiza kwambiri...kuwopa nthawi iliyonse ife tingazilole kutipulumuka.*

*Pakuti ngati mawu omwe anayankhulidwa ndi angelo anali okhazikika,...*

<sup>36</sup> Kodi inu mukuzimva Izo? “Ngati mawu omwe anayankhulidwa ndi angelo...” Tsopano, *mngelo* ndi “mtumiki.” Mawu okuti *mngelo* amatanthauza “mtumiki.” Ndipo tangodutsa kumene, mu bukhu loyamba apa, “Mulungu,

mu nthawi zamakedzana ndi mmayankhulidwe osiyanasiyana, ankayankhula kwa makolo mwa aneneri.” Awo anali atumiki a Mulungu. Ndipo iwo anali—awo anali atumiki a Mulungu. Iwo anali angelo a Mulungu. Mtumiki ndi mngelo; kapena mngelo ndi mtumiki, kani.

<sup>37</sup> Mtumiki! Inu ndi mtumiki, mmawa uno. Ndinu. . . Inu ndi mtumiki wa uthenga wabwino kapena mtumiki wa uthenga woipa. O, kodi izo si zokongola, kudziwa kuti ndife akazembe, kuti ndife angelo, atumiki a chiukitsiro? Ndipo ndife atumiki a Mulungu kwa dziko lodzaza tchimo, kuti Khristu ali moyo. Mu mitima yathu, Iye ali moyo. Mu mizimu yathu, Iye ali moyo. Ndipo Iye akutibweretsa ife kuchokera ku moyo wotsika wanyansi wa tchimo, ndipo akutikwezera ife mmwamba, ndipo akutipatsa ife “aleluya” mu solo yathu, ndipo akutipanga ife kukhala zolengedwa zatsopano. Ife ndi atumiki, angelo a Pangano. Kudabwitsa kwakeko!

<sup>38</sup> Ndipo tsopano, mu Chipangano Chakale, “Ng—ngati mawu oyankhulidwa ndi angelo anali okhazikika,” mwanjira imeneyo ankayenera kukhala ali olondola. Mu Chipangano Chakale, mawu a mneneri asanati awonetseredwe, iwo ankayenera kuti ayesedwe ndi kutsimikiziridwa. Iwo sanali olekerera ndi izo, monga ife tiriri lero.

<sup>39</sup> Kungotuluka panja ndi kukakhala ndi mtundu uliwonse wa zomverera kapena china chirichonse, “O, ulemerero kwa Mulungu, ndi umenewo!” Inu mukulakwitsa.

Baibulo linanena, kuti, “Mu masiku otsiriza, Mdierekezi azidzasanzira Chikhristu, mwapafupi kwambiri, mpaka izo zikanadzanyenga Osankhidwa omwe ngati nkotheke.” Ndi kulondola. Chotero, ife tiyenera kuti tiziyesa izo.

<sup>40</sup> Ndipo kodi iwo ankaziyesa motani izo mu tsiku lawo? Kwa Urimu Tumimu. Chapachifuwa cha Aaroni, chomwe chinali ndi miyala ija mwa icho: karbankulo, yaspi, daimondi, rube, safire. Miyala yonse iyo, yomwe imaimira kubadwa kwa mbadwa khumi ndi ziwiri zija, inali mu chifuwa cha Aaroni. Ndipo pamene mneneri ankalosera, ndi pamene Kuwala kopatulika uko kunkawalira apo, Mulungu amati, “Icho ndi Choonadi.” Koma, ziribe kanthu kaya izo ziwoneke ngati zenizeni chotani, ngati izo sizinawalire pa icho, izo sizinali Choonadi. Kotero, Urimu Tumimu iyo inapita ndi unsembe umenewo.

<sup>41</sup> Koma Baibulo ili ndi Urimu Tumimu ya Mulungu lero. Ndipo pamene mneneri alosera, izo ziyenera mwamtheradi kumathwanimira ndi Baibulo. Ndiye, Mulungu amayankhula, ndiye Iye amabwera pansu ndi kudzalitsimikizira Ilo.

<sup>42</sup> O, momwe ine ndingamulemekezere Mulungu lero! Ine ndikuganiza mobwereza mmawa wina Lamlungu, za pafupi monga izi, pamene ine ndinkachoka mu kachisi. Ndipo anthu inu munali mukulira ndi kumandifunsa ine kuti ndisapite. Koma,



pamene, ine ndinalalikira za Davide ndi Goliati, ndi momwe inu mukanati mukakomane ndi dziko lozizira, losayanjanitsika ilo lomwe limati masiku a zozizwitsa anatha.

<sup>43</sup> Ine ndinati, “Pali chimphona chimodzi chachikulu, ndipo mwamsanga pamene ife tichipha icho, ena onsewo atenga kulimbika.” Ndipo Ambuye anapereka icho. Ndiyeno apo panali Oral Roberts ndi Jagers, ndi ena otero, anasolola Lupanga, ndipo ife tinamenyana ndi mdani kumtulutsa mu dzikolo, tinatseka kamwa zawo. Iwo sangakhoze kunena kuti zozizwitsa sizikuchitika, chifukwa ndi izi apa. Zedi. Mawu a Mulungu ndi Amuyaya. Iwo anawalira pa Urimu. Anawalira pa Mawu, uyo ndi Urimu Tumimu Wake. Ndipo pamene iwo awalira pa Icho, izo zinali zovomerezeka.

Ndipo kwa aliynse yemwe ali wosowa, ngati ndinu wochimwa, inu mukufuna kuti mudziwe momwe mungapulumutsidwire, “Khulupirirani pa Ambuye Yesu Khristu.”

<sup>44</sup> Lero, ife tiri ndi zinthu zochuluka kwambiri zomwe iwe uyenera kuti uzizichita. “Uyenera kuti uzitembenuza masamba atsopano. Iwe uyenera kuti uzichita *izi* ndi kuchita *izo*, ndi cholinga choti upulumutsidwe.”

Ine ndikuganiza za woyang’anira ndende waku Filipi, pamene woyang’anira ndende uyu anamufunsa Paulo, “Kodi ndichite chiani kuti ndipulumutsidwe?”

Uyo akanakhala ali inu kapena ine, ife tikanamuuza iye zinthu zomwe iye *sakuyenera* kuti azichita. “Iwe uyenera kuti usiye kumwa. Iwe uyenera kuti usiye kuchita njuga kwako, kuchita njuga. Iwe uyenera kuti usiye *izi*. *Iwe* uyenera kuti usiye *izo*.”

Paulo sanamuuze konse iye zimenezo. Iye anangomuuza iye zinthu zomwe iye *akuyenera* kuti azichita. “Khulupirira pa Ambuye Yesu Khristu, ndipo iwe udzapulumutsidwa.”

<sup>45</sup> Tsopano, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine ali nawo Moyo wosatha.” Iyo ndi Urimu Tumimu ikuthwanima, Yohane Woyera 5:24. “Ine ndine Ambuye yemwe ndimachiza matenda anu onse.” Yakobo 5:14, “Itanani akulu, adzozeni mmafuta, pemphero la chikhulupiriro limupulumutsa wodwalayo.” Urimu ikuthwanima. Mukuona? Amenewo ndi Mawu Amuyaya a Mulungu.

<sup>46</sup> Ine sindikusamala amalingaliro awo angati, achikunja, osakhulupirira a Mulungu, openekera ati awuke. Mulungu aima ndi Mawu Ake. Iye analonjeza kuti Iye akanadzachita izo.

<sup>47</sup> “Ndipo ife tiyenera kuti tizipereka tcheru lochuluka motsimikiza kwa zinthu izi zomwe ife tazimva, kuwopa nthawi iliyonse ife tingazilole izo kutipulumuka. Pakuti ngati mawu

oyankhulidwa ndi angelo (aneneri) anali okhazikika . . .” Kuti iwo? Ife tikhoza kutha sabata pa izi.

<sup>48</sup> Kodi iwo anali okhazikika pamene Mose anawayankhula? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iwo ndithudi anali.

Nanga bwanji Eliya, ali pamwamba pa phiri? Ambuye anamuza iye, “Pita pamwamba apo, Eliya. Ine ndikakhala uko ndi iwe; ndikufuna chiyanjano china.” Mulungu amakonda kuyanjana ndi anthu Ake. Koma ife sitimakhala phee utali wokwanira kuti Iye achite chiyanjano ndi ife. Ife tiri otanganidwa kwambiri kulumpha lumpaha, kuchokera pa malo kupita ku malo, ndi zochulukwa kwambiri. “Khala bata, Eliya.” Iye ankafuna zaka zitatu ndi miyezi sikisi za chiyanjano. Ife sitingakhoze kumupatsa Iye maminiti atatu, nkomwe. Zaka zitatu ndi miyezi sikisi za chiyanjano chosalekeza. O, ine ndikuzikonda izo! Anati, “Usadandaule za kuphika; ife tiri nazo kale izo zokonzedwa. Akhungubwe azikudyetsa iwe. Ndipo chirichonse chikhala chiri bwino bwino. Ine ndikungofuna chiyanjano china.” Mneneri wakale uyu, Eliya, ali pamwamba pa phiri apo.

Pamene iye anali kuchita chiyanjano ndi Mulungu, bwanji, wolamulira anati, “Ine ndikukhulupirira ine ndikwera apo ndi kukamutenga iye.” Tsopano, musati muziyesera kuswa chiyanjano chimenecho.

<sup>49</sup> Chotero, wolamulirayo anadzapo, ndi ankhondo ake aakulu aamuna, a makumi asanu. Ndipo iye anati, “I—i—ine ndabwera kuti ndidzakutenge iwe, Eliya.”

<sup>50</sup> Ndipo Eliya anaimirira. Samalira, apa pali mneneri wa Ambuye! Iye anati, “Ngati ine ndiri wantchito wa Ambuye, siyani moto utsike kuchokera kumwamba ndi kukuwonongani inu.” Ndipo apo moto unatsika. Wolamulira anati . . .

<sup>51</sup> “O, inu mukudziwa chiani?” Mfumu, kani, inati, “Iyo inali mwinamwake—bingu, basi mphezi inayake imangodutsa apo, ndipo iyo inawakantha iwo. Ine nditumiza makumi asanu ena.”

<sup>52</sup> Eliya anaimirira, mmodzi wa angelo. Mawu ake ali okhazikika. Iye ankayenera kuti akhale wobwezera molungama kwa chirichonse chomwe chinachitidwa molakwitsa. Iye anati, “Ngati ine ndiri wantchito wa Ambuye, siyani moto ubwere.” Ndipo makumi asanu achiwiri anapsya. Chabwino. Kubwezera kulikonse!

*Pakuti ngati mawu omwe anayankhulidwa ndi angelo anali okhazikika, ndipo kulakwira kulikonse ndi kusamvera kunkalandira dipo lolungama . . .*

<sup>53</sup> Tsopano, apa pali chinthu chachikulu, ndime yotsatira.

*Tidzathawa bwanji ife, . . .*

<sup>54</sup> “Tidzathawa bwanji ife?” Ngati liwu la Eliya linabweretsa chiwonongeko, chifukwa iye anali mngelo wa Ambuye, ife

tidzathawa bwanji pamene Liwu la Khristu likuyankhula kudutsiramo? Kapena, ife tingalephere bwanji pamene inu mwapemphereredwa, ngati Ilo liri Liwu la Khristu? Ngati Khristu anawudzoza Mpingo Wake kuti uzipempherera odwala, ndipo Mpingo nkumachita zomwe Iye anati Iye...kuti iwo azichita, ndiye Iwo ungakhoze kulephera konse chotani Izo? Iwo sungakhoze. Inu mukhoza kulephera, koma Iwo sungakhoze kulephera. Ndipo bola ngati inu mukuwasunga Iwo, Iwo akudusitsani inu mopyola.

<sup>55</sup> Ngati inu mulephera, inu mulephera mwanokha. Inu mwangochokako ku Mawu. Koma bola ngati inu mukukhalabe ndi Mawu, Iwo sangakhoze kulephera. Pakuti mawu a aneneri ankachita *zakuti-n-zakuti*, ndi mochulukwa bwanji Mawu a Khristu ati akhale?

*Ife tidzathawa bwanji, ngati ife tinyalanyaza chipulumutso chachikulu chotero; chomwe pachiyambi chinayamba kuyankhulidwa kwa ife ndi Ambuye, ndipo chinatsimikizidwira kwa ife ndi iwo omwe anamumva iye;*

<sup>56</sup> Taganizani za Izo, zinayankhulidwa ndi Ambuye. Ndi nthawi zingati zomwe ife tikanati tibwerere mmbuyo? Kodi ife tikanati tiyime pati, apa pomwe kwa ora? Pamene Yesu anadza, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

<sup>57</sup> Tsopano, kumbukirani, poyamba zinayamba kuyankhulidwa ndi Yesu, Mwiniwake, ndipo kenako zinatsimikiziridwa ndi iwo omwe anamumva Iye. Tsopano mvetserani kwa Iye.

<sup>58</sup> Pamene Iye anadza ku dziko lapansi, Iye sankadzinenera kuti anali mchiritsi. Iye anati, “Si Ine yemwe ndikuchita ntchitozi; Ndi Atate Anga omwe akukhala mkati mwa Ine. Iwo akuchita ntchitozo. Mwana sangakhoze kuchita kanthu mwa Iyeyekha, koma zomwe Iye awawona Atate akuchita,” Yohane Woyera 5:19.

<sup>59</sup> Penyani pamene Filipino anadza kwa Iye. Nataniele... Kutachitika kutembenuka kwa Filipino, iye anapita ndipo anakamutenga Nataniele. Anati, “Tiye, ukamuwone Yemwe ife tamupeza: Yesu waku Nazareti, Mwana wa Yosefe.”

<sup>60</sup> Ndipo iye anati, “Kodi pangakhale kanthu kabwino kalikonse kangabwere kuchokera ku Nazareti?”

<sup>61</sup> Anati, “Tiye, ukawone.” Ndi momwe ungakhutitsidwire: tsimikizira Izo. Bwera ndi kudzawona. O, ndi zopambana zomwe ine ndinayamba ndazimvapo. Bwera ndi kudzadzipezera wekha. Usati uyime apo ndi kumatsutsa pa mzere wa kumbali. Koma, “Tsimikizira zinthu zonse, ndi kugwiritsa molimba kwa icho chomwe chiri chabwino.” Bwera ndi kudzawona.

62 Motsatira msewu iwo anapita, akuyankhula. Pamene iye anayenda napita mu kukhalapo kwa Ambuye Yesu, Iye anati, “Taonani M’Israeli mwa yemwe mulibe chinyengo.”

63 Izo zinachotsa khungu lonse pa iye, pafupifupi. Iye anayang’ana pozungulira, anati, “Chabwino, Rabbi, ndi liti pamene Inu munayamba mwandidziwa ine? Inu simunayambe mwandiwonapo ine. Inu mwandidziwa bwanji ine?” Filipino anatero. . .

64 “Usanati, pamene iye ankakuitana. . .” Anati, “Filipo asanakuitane iwe, dzulo, pamene iwe unali pansu pa mtengo wa mkuyu, Ine ndinakuwona iwe.” Ameni.

65 Iye anati, “Inu ndinu Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli.”

66 Mkazi anayenda napita mu Kukhalapo Kwake, ndipo Iye anati, “Pita, ukamutenge mwamuna wako.”

Iye anati, “Ine ndiribe aliyense.”

67 Anati, “Uko nkulondola. Iwe uli nawo asanu, ndipo yemwe iwe ukukhala naye tsopano si wako. Iwe wanena zooni.” Taganizani za izo.

68 Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri. Izo, ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzaza Iye adzatiuza ife zinthu zonse.”

69 Iye anati, “Ine ndine Iye, yemwe akuyankhula kwa iwe.”

70 Ndipo iye anathamanga ndipo anakawauza amuna a mu mzindawo, “Bwerani, mudzamuwone Mwamuna Yemwe wandiuza ine zonse zomwe ine ndimazichita. Kodi uyu si Mesiya amene?” Izo zinayankhulidwa ndi Ambuye.

71 Nchiani chinachitika? Yesu anati, Iye asanachoke, “Zinthu zomwe Ine ndikuzichita, inu muzidzachita aponso.” Nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] “Zinthu zomwe Ine ndikuzichita inu muzidzachita aponso, ngakhale zochuluka kuposa izi, pakuti ine ndikupita kwa Atate.” O, ine ndikukhoza kuwawona iwo pamene iwo anali kupita mtsogolo, kulikonse. Marko 16, “Akupita kulikonse, akulalikira; Ambuye akugwira ntchito ndi iwo, kutsimikizira Mawuwu.”

Ndipo apa, Paulo, akupereka chinthu chomwecho. Iye ananena kuti—Uthenga unayamba kulalikidwa ndi Yesu, ndipo unatsimikizidwira kwa ife ndi iwo omwe ankamumva Iye. Ndiwo Mwala wa Maziko. O, lidalitsike Dzina la Ambuye! Uwo ndi Mwala wa Maziko.

72 Ndipo kuganiza, zaka zikwi ziwiri zadutsa. Azawokha awuka, ndi achikunja, ndi openekera, ndi onyoza. Koma, lero, Yesu yemwe uja akutsimikizira Mawu Ake mwa chikhalidwe chomwecho mwa iwo omwe amamumvera Iye. “Kumumva

Iye,” sizikutanthauza kumva ulaliki chabe. Izo zikutanthauza, kumumva *Iye*. Inde.

<sup>73</sup> Kodi ife tidzathawa bwanji? Kothawira kwathu kuli kuti? O, inu mukuti, “Mulungu adalitsike, ine ndine wa mpingo wa Methodist. Ine ndine wa Presbateria. Ndine wa Chipentekoste.” Izo ziribe kanthu kamodzi kochita ndi Iwo. Ndipo inu mumapita ku mzere wakumbali ndi kumafuna kuchitcha Icho “zamizimu, kapena zina zowerenga maganizo, kapena mdierekezi wina,” kapena chinachake. Manyazi pa iwo!

<sup>74</sup> “Ngati mawu aliwonse anali okhazikika a angelo . . .” Yesu anati, “Izo si . . . Kanthawi pang’ono, ndipo dziko silindiwona Ine kenanso. Komabe, inu muzindiwona Ine, pakuti Ine ndizikhala ndi inu, ngakhale mkati mwa inu, mpaka kumathero a m’badwo.” Ndipo pamene ife timuwona Iye akubwera pansi, kuti adzapitirize kutsimikizira Mawu Ake, ife tidzathawa bwanji ngati ife tikuyamwira kwa mpingo wina, kapena bungwe lina, kapena chipembedzo, kapena nthano zina zopeka zathu zathu? Inu kulibwino mumasuke. “Pakuti tchimo lililonse linkalandira chilango choyenera pansi pa angelo, ndi mochuluka bwanji pamene Mwana wa Mulungu akuyankhula kuchokera Mmiyamba, kuti awonetsere Mawu Ake! Kodi ife tidzathawa bwanji, ngati ife tinalanyaza chipulumutso chachikulu choterechi?” O, mai! “Mulungu nayenso . . .”

Ndime ya 4:

*Mulungu nayenso powachitira iwo umboni, . . .*

<sup>75</sup> Penyani izi. Ambuye ankachitira maumboni. O, ine ndiri wokondwa kwambiri pa izo! Ambuye ankachitirapo umboni.

<sup>76</sup> Penyani. Pamene Eliya anakhala pa phiri, ndipo iye anati, “Ngati ine ndiri munthu wa Mulungu, siyani moto ugwe kuchokera Kumwamba ndipo ukutheni inu.” Mulungu anachitira umboni kuti iye *anali* munthu wa Mulungu.

Mulungu nthawizonse amachitira umboni. Moyo wanu uzichitira umboni. Ine sindikudziwa chomwe umboni wanu uli, koma moyo wanu umayankhula momveka kwambiri, mawu anu sangakhoze kumveka. Koma, momwe—mumakhalira, moyo wanu wa tsiku ndi tsiku umachitira umboni chomwe inu muli. Mulungu amachitira umboni. Inde. Mzimu Woyera ndi chizindikiro, ndipo chizindikiro chimatenga mbali zonse za pepala. Iwo amakuwonani inu mutaima *apa* ndipo amakuwonani pamene inu mukuchokapo. Osati mu tchalitchi mokha koma pa ntchito ya tsiku lililonse. Ndinu osindikizidwa kumbali zonsezo, mkati ndi kunja. Ndi chisangalalo chomwe inu muli nacho, ndipo ndi moyo umene inu mumaukhala, inu mwasindikizidwa, mkati ndi kunja, mwakuti inu mukudziwa kuti inu munapululumutsidwa ndipo dziko limadziwa kuti ndinu opulumutsidwa, ndi moyo umene inu mumaukhala, pakuti

Mulungu amachitira umboni. Lidalitsike Dzina Lake Loyera! Mai, ine ndikumverera mwachipembedzo!

<sup>77</sup> Taganizani za izo, abale, uko. O! “Nkhosa Zanga zimamva Mawu Anga, ndipo mlendo izo sizingamutsatire.” O, momwe kuti maina athu ali pa zikhatho za manja Ake! Iwo ali pamaso pa Iye, usana ndi usiku. Mawu Ake ali nthawizonse patsogolo Pake, Lonjezo Lake. Iye sangakhoze kuziiwala izo. Ndipo Iye amakukondani inu.

<sup>78</sup> Tsopano, Iye aziwachitira umboni Ake omwe. Inu simumatsegula kamwa yanu kuti munene mawu, dziko lizidziwa kuti chinachake chinachitika kwa inu.

*...kuchitira umboni, zonse mwa zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi mwa zozizwitsa zosiyanasiyana, ndi mphatso za Mzimu Woyera, molingana ndi chifuniro chake chomwe?*

<sup>79</sup> Tiyeni ife titenge Lemba limodzi lokha tsopano tisanati titseke; pa Tsiku la Pentekoste, pamene iwo analandira Mzimu Woyera. Pafupi masiku anai mtsogolo, Petro anali atadutsa mu chipata chotchedwa Chokongola; iye ndi Yohane. Iwo anati, “Tayang’ana pa ife,” kwa mwamuna. Ndipo iye anati, “Siliva ndi golide ine ndiribe, koma zomwe ine ndiri nazo ine ndikupatsa iwe. Mu Dzina la Yesu Khristu waku Nazareti, dzukapo ndi kuyenda.” Ndipo bamboyo anayang’ana mmwamba ndipo sanafunse kanthu ka izo. Iye anangoimirira ndipo anapita akuyenda. Awo anali mbuli ndi amuna osaphunzira. Koma Baibulo linati, “Iwo anayenera kuti awamvere iwo, pakuti iwo anadziwa kuti iwo anakhala ali ndi Yesu.”

<sup>80</sup> M’bale, pamene dziko lidziwa kuti inu mwakhala muli ndi Yesu, pamene inu mungakhoze kumakhala moyo wosaipitsidwa choterowo mu dziko lapakali panoli ndi mu mdima uwu, mwakuti dziko nkudziwa ndi kumakhoza kuwona kuti inu munakhala muli ndi Yesu; pamene wachiwerewere wokhukhuluzika, wanyansi wamu msewu angakhoze kukhala dona, atatsukidwa mu Magazi a Mwanawankhosa; Mulungu nkumachitira umboni kuti Iye alimoyo.

<sup>81</sup> Kumutenga chidakhwa, yemwe ali wotsika pansu kwambiri yemwe angamamuzembere mkazi wake, yemwe iye angamawazunze ana ake, ndi kuchotsa chakudya cha pa gome, kuti akaziwonongere pa wachiwerewere. Mumusiye iye akomane ndi Yesu kamodzi. Inu mudzamuwona iye akubwerera, ngati Legio, yemwe anali mmalingaliro ake abwino ndipo atavekedwa, kwa ana ake ndi kwa mkazi wake ndi kwa okonedwa ake. Ndithudi.

<sup>82</sup> Nthawi ina pakale, pafupi zaka forte zapitazo, pamene zipembedzo za mdziko zinakomana, ndipo osiyanasiyana anadzuka apo ndipo anayankhula. Ndipo Achimuhamadi anayankhulira chipembedzo cha Chimuhamedi. Achiyane

anayankhulira Ayane; Achibudda anayankhulira aBudda. Ndipo dotolo wamng'ono, ine ndaiwala lomwe dzina lake lotsiriza linali, pa nthawi ino yokha. Ine ndimalidziwa dzina lake, koma ine ndaliwala ilo. Iye anayankhula kuyimira Chikhristu. Ndipo iye ananena nkhani ya Dona Maccabee waku Oklahoma, mu America.

Iye anali wamakhalidwe oipa kwambiri ndipo wotsika pansu kwambiri, mpaka ngakhale pamene iwo ankapita kuti akamuphe iye, iwo sakanaka ngakhale manja awo pa iye, iye anali woipa kwambiri ndi wauve. Iwo anali atamumanga iye pa mulandu: kusuta ndudu; kuyendetsa ngolo ya akavalo; ndipo anaswa m—m—malamulo, zolembedwa mu Oklahoma, pamene iye ankadutsa mu msewu, akuyendetsa mitu inai ya akavalo. Ndipo iye anali woipa kwambiri ndi wauve kwambiri mpaka akumeneko sankakhoza ngakhale kuyandikira kumene iye anali; mochulukwa kwambiri, mpaka pamene onyonga ankati amunyonge iye, iwo sakanati amunyonge iye. Iwo anangotsanulira phula ndi nthenga pa iye, kuti amuphe iye.

Ndipo pamene mlaliki wamng'ono uyu anapereka nkhani yake, mwanjira yotero, mpaka iye anawapangitsa anthu kukhala pansonga za mipando yawo, kuti amvetsere zomwe zikanakhala zotsatira. Pamene iye anafika kwa izo: woipa kwambiri, wauve, wotsika-pansi, mpaka malamulo sakanakhoza konse kupusa ndi iye, iye anali wotsikitsitsa kwambiri. Mdierekezi yemwe mu gehena akanati amukane munthu woteroyo, pafupifupi, momwe iye anakambira nkhaniyo. Ndiye iye anati, “Njonda, za zipembedzo za mdziko, kodi chipembedzo chanu chiri ndi chirichonse chomwe chingayeretse manja a Dona Maccabee?”

<sup>83</sup> Aliyense anakhala bata. Ndiye iye anawomba manja ake palimodzi, ndipo analumphira mmwamba mu mlengalenga. Iye anati, “Ulemerero ukhale kwa Mulungu! Magazi a Yesu Khristu sangatsuke manja ake okha, koma Iwo angatsuke mtima wake ndi kumupanga iye Mkwatibwi Wake.” Ndikukuuzani inu:

Chisomo chodabwitsa! nkhani yokoma  
kuimva,  
Chomwe chimapulumsa wopandapake  
wonga ine!  
Ine poyamba ndinali wotaika, koma tsopano  
ndapezeka,  
Ine ndinali wakhungu, koma tsopano  
ndikuwona.

Ndi chisomo chimene chinaphunzitsa mtima  
wanga kuchita mantha,  
Chinali chisomo chinachotsa mantha anga;  
Momwe chisomo icho chinawonekera  
chofunika  
Ora lomwe ine ndinakhulupirira koyamba!

<sup>84</sup> Ndithudi. “Kodi ife tidzathawa bwanji, ngati ife tinalanyaza zoterezo?” Inu mukanyalanyaza kudya, inu mufa. Inu mukanyalanyaza potembenuka pa ngodya, inu muchita ngozi. Inu mukanyalanyaza kuti muikame mkaka ng’ombe, iyo iyamba kuuma. Inu mukawanyalanyaza mano anu, inu mudzachotsamo onse awo. Ndithudi. Inu mudzalipira chifukwa cha kunyalanyaza kwanu.

<sup>85</sup> O Branham Tabernacle ndi inu alendo, ndiloleni ine ndikuuzeni inu chinachake tsopano. Inu mukanyalanyaza kuchitira umboni za ulemerero wa Mulungu, inu mukanyalanyaza kumupatsa Mulungu matamando ndi ulemerero, inu mudzadzipeza nokha mutazizira, kufunda, ndi kubwerera mmbuyo, limodzi la masiku awa. Inu muzimupatsa Mulungu matamando. “Kodi ife tidzathawa bwanji, ngati ife tinalanyaza chipulumutso chachikulu choterechi?”

<sup>86</sup> Tikufika pochedwa. Ine ndangopezeka kuti ndamuzindikira, M’bale Toms akulowa muno kumbuyo uko. Ife titseka ndi kudzapitiriza izi usiku uno, Ambuye akalola.

Tiyeni ife tipemphere kamphindi kokha.

<sup>87</sup> Atate athu Akumwamba, kwa Inu kukhale madalitso, ndi matamando, ndi ulemu, ndi ulemerero, ndi nzeru, ndi ukulu, ndi mphamvu, kwa nthawi ndi nthawi. O, kwa Mwanawankhosa uyo yemwe ali pa Mpandowachifumu, ulamuliro ndi maufumu ndi chirichonse chinaperekedwa kwa dzanja Lake. Pamene Iye anauka kuchokera kwa akufa, kuti atilungamitse ife, Iye anafuulira kwa dziko, “Mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi zaperekedwa kwa dzanja Langa. Pitani inu, chotero, ku dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga.”

O Mwanankhosa wakufa, Magazi Anu ofunika  
Sadrataya konse mphamvu Yake,  
Mpaka Mpingo wonse woomboledwa wa  
Mulungu  
Udzapulumsidwe, ndi kusadzachimwanso.

<sup>88</sup> Tithandizeni ife, monga atumiki, kuti tiwone kuti ife tikusowa zochuluka kwambiri; momwe ife tiyenera kukhala ndi mpingo, ife tiyenera tikhale ndi *ichi*, ife tiyenera kukhala ndi chirichonse.

<sup>89</sup> Akazi athu, asanapite ku mpingo, iwo apobe akudzitcha okha Akhristu, amasowa kuti akhale ndi mtundu wina wake wa diresi, kapena ayenera kuti avale mophambika.

Ndipo alaliki amayenera kuti akhale ndi ndalama zochuluka kwambiri iwo asanati abwere, ndipo chirichonse chiyenera kuti chikhale *mwakuti-n-mwakuti*.

<sup>90</sup> O Khristu, pamene ine ndimawerenga apa, “Momwe iwo ankayendera, mu zikopa zankhosa ndi zikopa za mbuzi, ankakhala mu timakhumbi ta mu nthaka, ndi mmphanga.”



Iwo ankayendayenda, pansi pa kuzunzika koipa, ndipo, apobe, anasunga Chikhulupiro, pansi pa utumiki wa angelo. Kodi ife tidzathawa bwanji, pamene Ambuye Yesu atipatsa ife manyumba abwino, ndi magalimoto, ndi zovala, ndi chakudya? Ndipo ife timang'ung'uza. Ife timakhala pomwepo. Ndife aulesi. Ife sitimayesera konse kupita kunja ndi kukachita chinachake cha izo. Kodi ife tidzathawako bwanji, Mulungu?

<sup>91</sup> O, ine ndikupemphera kuti Inu muwotche kukhuza kwachikale mu mtima uliwonse, mmawa uno, Ambuye, kuti anthu akhoze kudzuka ndi kukhala pa icho. Tiloleni ife tizigwira ntchito pamene kuwala kwa tsiku kukuwala, chifukwa dzuwa likulowa mwamsanga. Ndipo chitukuko chikupita, ndipo sipadzakhalanso nthawi. Iyo idzalowererana mu Muyaya.

<sup>92</sup> O Mulungu, perekani lero kuti ife tipite ndi masomphenya atsopano, ndi nzeru, ndi kumvetsa, kuti tizidziwa momwe tingafikire kwa ochimwa ndi kuwabweretsa iwo kwa Khristu. Imvani pemphero la wantchito Wanu, Ambuye.

<sup>93</sup> Ine ndikupempha, ngati pangakhale wina aliyense pano, yemwe sakumudziwa Khristu ngati Mpulumutsi wawo, kodi inu mungakweze dzanja lanu nkuti, “Ndikumbukireni ine, M'bale Branham”? Kodi inu mungangokweza dzanja lanu, nkuti, “Ndikumbukireni ine. Ine ndikufuna kuti ndikhale Mkhristu. Ine sindikufuna kuti ndizinyalanyaza mopitiriranso”? Mulungu akudalitseni inu, kumbuyo uko, bwana. Wina wakenso? Mukuti, “Ine ndikufuna kuti ndikweze dzanja langa, M'bale Branham. Ndipo ine ndikufuna kumulandira Khristu, ngati Mpulumutsi wanga, ine ndanyalanyaza, nthawi zonse. O, ine ndimapita ku mpingo, zedi, ine ndine wa mu mpingo.”



*BUKHU LA AHEBRI*

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)